Baibulo ya ana

Ikupasilani

Nowa ndi madzi amphamvu osefukila

Yolembedwa ndi: Edward Hughes
Yojambulidwa ndi: Byron Unger; Lazarus Alastair Paterson
Yotengedwa ndi: M. Maillot; Tammy S.
Yotathauzidwa ndi: Phiri Williams
Yo pangidwa ndi: Bible for Children
www.M1914.org

BFC
PO Box 3
Winnipeg, MB R3C 2G1
Canada

©2020 Bible for Children, Inc.
Chilolezo: Muli ndi ufulu wotenga ndi kuchurukitsa makopewa koma osagulitsa.

Nowa anali munthu amene analambira Mulungu. Wina aliyense anali Kusamvera ndi kudana ndi Mulungu. Tsiku lina, Mulungu ananena mawu odabwitsa. "Ndidzaononga dziko ili ndi kuipa kwake," Mulungu anamuuza Nowa. "Ndi banja lako lizapulumuka basi."



Mulungu anamuchenjeza Nowa kuti kudzakhala chigumula cha madzi ndikukwanila dziko lonse lapansi. "Manga chombo, ngalawa yaikulu yokwanila banja lako ndi nyama zambiri," ndipo Nowa analangizidwa. Ndipo Mulungu anampatsa Nowa malangizo wowonjezera. Nowa anatangwanika kwabasi!



Ndipo anthu anamuseka Nowa monyoza kuti chifukwa chiyani ukupanga chombo.

Koma Nowa sanasiye kupanga chombo. Iye anapitiliza kuwauza anthu za Mulungu. Koma panalibe omvera.

Nowa anali
ndi chikhulupiliro
chachikulu. Anakhulupirila
Mulungu ngakhale madzi
otero sanayambe abwelapo.
Posatenga nthawi
chombo chinakhala
chokhonzeka
kutenga
zinthu.

Kenaka nyama zinabwera. Mulungu anabweretsa mitundu isanu ndiziwiri zamtundu wina, ziwiri za mtundu wina mbalame zazikulu ndi zazin'gono, zilombo zazin'gono ndi zazikulu zinapezeka kulowa muchombo.

Ngakhale anthu anamseka namnyozera Nowa pomwe ama lowetsa nyama. Anthu sanasiye kumuchimwira Mulungu. Iwo sanampemphe kulowa nawo mchombo.



Pomaliza, nyama zonse ndi mbalame zinalowa.



"Lowani mchombo," Mulungu adawa itana. "Iweyo ndi banja lako basi." Nowa, mkazi wake, ana ake atatu ndi akazi ake analowa mchombo. Kenaka Mulungu anatseka chitseko!



Kenaka mvula inabwela.
Thamanda lodabwitsa linabwera
padziko lapansi kwa masiku
makhumi anayi ndi usiku.

Chigumula cha madzi chinagwa kumizinda ndi kumidzi. Pamene mvula inasiya, ngakhale mapiri anali odzala ndi madzi. China chilichonse chopuma chinafa.



Pamene madzi anakwera, chombo chidayandama pamwamba. Mwina munali mudima mkati mwa chombo, mwina mabampu, mwinanso kuopsya. Koma chombo chinamvundikira Nowa kuchigumula.


Patatha masiku asanu achigumula,
Mulungu anatumiza mphepo yowumitsa
madzi. Pan'gono pan'gono chombo
chinabwera ndikukhala pamwamba pa
mapiri a Ararat. Ndipo Nowa
anakhala mkati mwa
chombo kwa
masiku
makhumi
anayi
pomwe madzi
amaphwa.

Ndipo Nowa anatumidza makungubwi ndi nkunda kuchoka mchombo paka dzenera kakan'gono



anatsegura. Sanapeze malo owuma kuti apume, kenako nkunda inabwelera kwa Nowa. Patatha sabata imodzi, Nowa anayesanso. Nkhunda inabwerela ndi tsamba kukamwa. Sabata yinayo Nowa anadziwa kuti dziko lauma chifukwa nkunda siinabwererenso.

Mulungu anauza Nowa kuti ndinthawi yoturuka mchombo. Nowa pamodzi ndi banja lake anaturutsa nyama zonse mungalawa.

Ndichimwemwe chotani Nowa anakhala nacho! Ndipo anamanga guwa ndi kupembedza Mulungu amene anawa pulumutsa kuchigumula ndi banja lawo.


Mulungu analonjedza Nowa lonjezo lopambana. Kuti Mulungu sadzabweretsanso chigumula cha madzi kuweruza
machimo ya anthu. Ndipo Mulungu anapereka chikumbutso cha lonjezo uta waleza kukhala chizindikilo.

Nowa ndi banja
lake anayambanso
moyo watsopano chitatha
chigumula. Ndipo mtundu
wadziko lapansi unchokera
kwa Nowa ndi ana ake.

Nowa ndi madzi amphamvu osefukila

Nthano yochokera mu mau a Mulungu, Baibulo,

opezeka mu

Genesis 6-10

“Polowela pa mau anu pamapasa kuwala.”
Masalimo 119:130

Mapeto

Nthano iyi yamBaibulo imakamba za ubwino wa Mulungu yemwe anatipanga ndipo akufuna kuti mumdziwe iye.

Mulungu amadziwa kuti tima chita zoipa, zimene zimachedwa chimo. Chilango cha uchimo ndi infa, koma Mulungu anatikonda kwambiri ndipo anatuma mwana wake yekha, Yesu, kuzatifela pamtanda ndi kunzunzika chifukwa cha machimo anu. Ndipo anaukanso kwa akufa na pita kumwamba! Ngati ukukhulupirira Yesu mupempheni akukhululukileni machimo anu, azakukhululukirani! Adzabwera kukhala nanu, ndipo muzakhala naye kunthawi zonse.

Ngati mukukhulupirira kuti izi ndizoona, nenani ichi kwa Mulungu: Ambuye Yesu, ndikhulupirira ndinu mwana wa Mulungu, ndipo munakhala munthu kundifera ine machimo yanga, ndipo mulinso ndi moyo. Chonde, lowani mmoyo mwanga ndikundi khululukira machimo anga, kuti ndikhale ndi moyo watsopano, ndipo tsiku lina ndikakhale ndiinu muyaya. Ndithandizeni kukumverani ndi kukhala mwa inu ngati mwana wanu. Ameni.

Welenga Baibulo ndi kuyankula ndi Mulungu matsiku onse!
Johane 3:16